PRIORITY
PAR AVION
BY AIR MAIL



Bweranikwa Ine
LELO
Mateyu 11:28

# Kalata ya Inu

**ISBN 978-3-96162-195-8**

© 2025 by GBV Dillenburg GmbH
www.gbv-dillenburg.de
www.gbv-online.org
www.bibleo.org

Ulemu wa
Verbreitung der Heiligen Schrift, www.vdhs.com

Malemba anatengedwa mu Revised Nyanja Union Version
© Bible Society of Malawi, Blantyre 1992

Printed in Germany

© photos: p. 11 l.: Daniel Ernst, stock.adobe.com; p. 11 r.: Diversity Studio, stock.adobe.com; p. 46: Renate Wefers, stock.adobe.com; others: panthermedia.net, et al.



# Kwa Inuyo nokha

Mmanja mwanu mwanyamula kalata ya padera imene ikufuna kukulankhulani inuyo nokha. Mwina mutha kuganiza: "Malemba analembedwa pa pepalawa si akalekale?" Ndi zoona. Mauthenga a pafoni kapena maimelo akugwiritsidwa ntchito m'malo mwa makalata.

**>> Koma ngakhale mu mzaka za digito, ndikofunikirabe kulemba zolemba zapadera pa mapepala monga njira yowonetsera mtengo wake ndi kufunikira kwake.**

Chonde khalani ndi nthawi ndi Kalata iyi yapadera yomwe mwayinyamulayi. Ndiyofunikira kwambiri. Choncho iwerengeni mosamala. Simudzakhumudwa nayo!

**Mudzapeza mawuthenga odabwitsa a za**

- **ina, kalata yamtengo wapatali kwambiri**
- **kalata ya tanthawuzo kwambiri mu dziko lapansi**
- **uthenga waukulu kwambiri wa nthawi zonse ndi kusangalatsa kodalilika ndi kufunikira kwake ku nyengo ino.**



## Kalata iyi ya mtengo wapatali kwambiri, Baibulo, ndi uthenga wanu, wochokera kwa Mulungu mwa chindunji.





# Baibulo - Kalata ya Inu

## Baibulo lili ngati Kalata ya pa ndege – kochokera kwake ndi kumwamba.

**Mulungu ndi mulengi wodabwitsa wa chilengedwe.**

**Iye anakupatsani inu moyo wanuwo ndipo amakudziwani kwathunthu. Inu simunangopangidwa mwa mwayi ayi!**

**Iye akufuna ubale ndi inu ndipo akupanga chionetsero chachindunji cha chikondi kwa inu kudzera mu 'kalata' Yake.**

Simunayidziwe Kalata ya Mulungu? Kapena inayikidwa mu nyumba mwanu pena pake, osawerengedwa.

Inu simumangoyika padera kalata yanu mosasamala motero. Mumayiwerenga ndi chidwi chachikulu. Choncho, tsekulani Kalata ya Mulungu ya kwa inu – werengani Baibulo!

Inu mudakalibe Baibulo? Tidzakhala osangalala kukutumizirani limodzi Kwa ulele.

Kumapeto kwa kabuku aka mupeza momwe mungalumikizilane ndi ife.





# Kalata yapadera

Inde, mwadziwa bwino: Baibulo, mawu a Mulungu, akutanthawuza pano, pa mutu wakuti “Kalata ya Inu” ukugwirizana bwino. Chifukwa Kalata iyi yosowa ndi yofunikira kwambiri chifukwa Mulungu ndiyemwe analemba.

Mungathe kutsutsa: “Koma Baibulo linalembedwa zaka mazana mazana apitao pafupifupi ndi anthu 40 osiyana-siyana. Kawiri-kawiri, ngakhale mayina awo satchulidwa.”

**Eya, ndi zoona. Mulungu anawuzira uthenga wake kwa anthu payekha payekha mwa chindunji:**



**Pakuti kale lonse chinenero sichidadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu ogwidwa ndi Mzimu Woyera, anayankhulidwa.**

Baibulo – 2 Petro 1:21

Mulungu adagwilitsa ntchito maluso awo, maphunziro awo, chikhalidwe chawo, kochokera kwawo ndipo ngakhale kalembedwe kawo.

*>>> Analemba liwu ndi liwu zomwe Mulungu ankafuna kuti azilembe iwo.*

Ichi chimatchedwa “kuwuzilidwa”.

## Mabuku a m’Baibulo

- Baibulo lili ndi magawo awiri:
  - chipangano chakale (Mabuku 39)
  - chipangano chatsopano (Mabuku 27)

- Chipangano chatsopano chili ndi:
  - Mauthenga abwino anayi
  - Machitidwe a tumwi
  - makalata makumi awiri ndi imodzi (21)
  - Chibvumbulutso

Baibulo limakupatsani mayankho ku mafunso a moyo.

Kudzera mu kuliwerenga, inu muli ndi mwayi kukumana ndi kusintha kwabwino kumene chikondi cha Mulungu chingabweretse pa moyo wanu.

Genesis
Eksodo
Levitiko
Numeri
Deuteronomo
Yoswa
Oweruza
Rute
1 Samueli
2 Samueli
1 Mafumu
2 Mafumu
1 Mbiri
2 Mbiri
Ezara
Nehemiya
Estere
Yobu
Masalmo
Miyambo
Mlaliki
Nyimboya Solomo
Yesaya
Yeremiya
Maliro
Ezekieli
Danieli
Hoseya
Yoweli
Amosi
Obadiya
Yona
Mika
Nahumu
Habakuku
Zefaniya
Hagai
Zekariya
Malaki

Mateyu
Marko
Luka
Yohane
Machitidwe
Aroma
1 Akorinto
2 Akorinto
Agalatiya
Aefeso
Afilipi
Akolose
1 Atesalonika
2 Atesalonika
1 Timoteyo
2 Timoteyo
Tito
Filemoni
Ahebri
Yakobo
1 Petro
2 Petro
1 Yohane
2 Yohane
3 Yohane
Yuda
Chibvumbulutso



## "M'badwo – wozondoka Mutu"

Ndinunso a m'badwo uwu? Kapena mawu awa sakutanthawuza kanthu kalikonse kwa inu? Kodi nthawi zonse mumakhala mutu wozondoka, chidwi pa lamya lanu la m'manja kapena pa tabuleti?

Kukhala pa layini kawiri-kawiri ndipo kwina kulikonse kumakutsogolerani ku kumizidwa ndi kusefukira kwa mawuthenga ochokera pa intaneti. Pali china kodi kupatula kufufuza, kucheza ndi kutumiza mawuthenga? Ma ola akupita mosadziwika ndipo nzeru zanu zapanikizidwa – ndipo sizilizowonekera kwambiri kuti moyo wanu waonongeka. Osati ichi chokha, koma chosokoneza ichi chimakusunganibe kukuganiza za Mulungu ndi uthenga Wake wa kwa inu.

**Mfundo:** Ngati mukufuna kudziwa mulungu panokha, simungapite kudutsa Baibulo. Mukusowekera bata kuzungulira inuyo kuti muliwerenge. Choncho zimitsani chili chonse chomwe chingakusokonezeni mu dongosolo limeneli. Mudzadabwitsidwa momwe ichi chidzachitire bwino inu. Malingaliro anu adzakhudzika mu njira yabwino, yangwiro yomwe simunakumanepo nayo ndi kale lomwe. Powerenga Baibulo, mudzatha kupeza choonadi ndi kudziwa wina amene ali ndi chidwi ndi inuyo, amene amakukondani ndi amene akufuna kupatsa moyo wanu tanthawuzo lozama ndi cholinga cha mphoto.

Pa masamba awa 62 ndi 63 mudzapeza mfundo pa momwe mungawerengere Baibulo.

**Chonde lipatseni mpata!**



# Kodi Baibulo ndi la posachedwapa?

**Anthu ambiri amakhulupilira kuti ndi chopusa kuchita ndi "buku la nthawi zakale lotha fasho." Ali amaganizo akuti munthu wamasiku ano sangakhulupilirenso Baibulo.**

**Maganizo ngati amenewa kawiri-kawiri amathandizidwa ndi ofalitsa nkhani ndipo amalandiridwa opanda mafunso.**

**Komabe, ndi maganizo olakwika onena kuti m'mene zinthu ziyenera kukhalira ndi nzeru zikuyenera kukana Baibulo.**

**Pa masamba osatirawa mudzapezamo mfundo zambiri zimene zikutsimikiza kufunika ndi tanthawuzo la Baibulo.**

**Odala iwo akumva mawu a Mulungu ndi kuwasunga**

Baibulo – Luka 11:28

# Kugwilizana kwa chozwizwa



Mmodzi mwa omwe ndimamudziwa ndi woimba ndipo amatha kusewera zida zingapo. Iye amagwiritsa ntchito kompyuta yake kujambula mawu ndi kupanga zina ndi zina zokhudzana ndi ntchito yake.

Iye anafotokoza: "Poyamba, Ndimatenga chida changa ndikuyimba sapulano. Ichi chimajambula nyimbo koyamba.

Pa kuyimba kwachiwiri ndi majambula oloto popanda kufufuta kujambula koyamba kuja. Umu ndi momwe ndimaphatkizira zida zina zisanu ndi chimodzi, mpaka ku besi lozama kwambiri.



Kenako nyimbo zomveka zisanu ndi zitatu zimabwe-retsedwa pamodzi. Kodi mukufuna kumva zotsatira?"

Chomwe ndinamva chinali cha mamvekedwe a ulemelero. Ndikovuta kukhulupilira kuti woyimba m'modzi angakwani-tse izi!

Iyi ndi nkhani yomweyo ngati baibulo. Linalembedwa ndi anthu oposa makumi anayi (40) osiyanasiyana. Onse anawuzilidwa ndi woyimba wosayerekezeka, Mulungu, Mzimu Woyera, Iye anapanga "zida" zonse izi 40 kuziyimba.

**Buku lili lonse la m'baibulo lili ndi chikalidwe chake, koma limagwilizana mwa umodzi ndi onse pamodzi malingana ndi dongosolo la Mulungu.**

**Ichi ndi chimodzi mwa zodabwitsa za Baibulo!**

**>>> Werengani Baibulo kuti mupeze mgwirizano wake wapadera dera!**





# Kudikirira pachabe...

M'bambo, yemwe sankasamala nkomwe za Baibulo, ankafuna kumnyengelera mkhristu wachichepere kuti Baibulo linatha ntchito ndipo ndilosokoneza ku zopezeka za masiku ano. Iye anafuna kumutumizira iye zolemba zina zosankhidwa kuchokera ku sayansi ndi zakaganizidwe zokhudza phunziro ili.

Wachinyamata uyu,komabe, sanagwedezeke mu chikhulupiliro chake. Iye anayankha: ''Ngati muli ndichina chake **chabwino chosiyana ndi chiphunzitso cha pa Phiri** (Mateyu 5-7), chilichonse **chabwino kusiyana ndi nkhani za Msamariya wachifundo, mwana wolowelera, kapena Mzimayi pa chitsime cha Sukari** (Luka 10 ndi 15, Yohane 4); ngati muli ndi china chili chonse **chotonthoza kwambiri kusiyana ndi Masalmo 23** kapena kudziwa china chili chonse chimene **chikuvumbulutsa chikondi cha Mulungu kwa ine chabwino kusiyana ndi mphatso ya mwana Wake Yesu Khristu**, kapena mungathe kunditumizira msanga chili chonse chomwe **chikufotokoza momveka bwino muyaya wa mtsogolo**

Iye anadikira yankho pachabe

**Palibe buku lina lomwe lingafanizilidwe ndi Baibulo. Chifukwa chake ndi chosavuta: Baibulo ndi buku la Mulungu.**

# Kodi baibulo linabwera bwanji kwa Ife

**Bwanji, ndipo anthu analemba zokhudzana chiyani?**

3000 BC

Ngati wina aliyense ankafuna kulemba ''kalata'' mzaka 5,000 zapitazo, iye samalemba ndi pepala ndi inki. Anthu amagwiritsa ntchito zotchedwa Kunifomu m'masiku amenewo – zizindikiro ndi zithunzithunzi zimene zima wumbidwa mu dothi lochepa m'mapale, amene amawumitsidwa kapena kuwotchedwa. Mu nthawi ya kufufuza mu mizinda yakale lerolino ku Siriya ndi ku Iraki, zikwi zikwi za mapale a dothi okhala ndi zolemba zimenezi zidapezeka.







1500 BC

Pafupi fupi nthawi imodzi, Aigupto anapanga zolemba zosiyana zojambula ndi zophiphilitsa (heyirogilayifiki), zomwe tingazipenzenso mu mapiramidi. Zinatengera odziwa zilankhulo za make dzana kutanthawuzila zolemba za zilankhulidwezi zakalekale za anthu.

Malembedwe awa adali ndi zoipa zazikulu: amakhala ndi mazana a zizindikiro. Munali mu 1500 BC m'mene zilembo zinapangidwa.

1000 BC

Ndi kusintha kochepa, zilembo izi zinafalikira mwansanga kuchokera 1000 BC. Ndi maziko a zilembo zathu za Chilatini, zimene zikugwilitsadwabe ntchito lero.



Kupatula dothi, miyala kapena matabwa, anthu pambuyo pake anayamba kulemba pa magumbwa (Papyrus). Pambuyo pake, anthu amalemba pa zikopa (zopangadwa kuchokera ku nyama), zimene zimapangidwa mu mipukutu.



**Umu ndi momwe Mulungu adasamalirira modabwitsa kuti panthawi yomwe Baibulo linalembedwa, panali kaundula wosavuta, zomveka zolembedwa zomwe zilipo.**

**Kulemba, kusonkhanitsa ndi kusunga**

Mose anali m'modzi mwa anthu oyamba kulembedwa m'baibulo. Timawerenga kangapo kuti Mulungu adampatsa iye ntchito yolemba m'bukhu zinthu zomwe zidachitika.

Kudzera mwa anthu osankhidwa ndi Mulungu, mabuku osiyanasiyana a Chipangano Chakale anali kutoleledwa ndi kusungidwa mosamala.

400 BC

Pafupifupi 400 BC CHIPANGANO CHA KALE chidamalizidwa. Chidalembedwa mchilankhulo cha Chihebri, ndi masamba ochepa m'Chiaramu.

100 AD

Kunali kokha kuyambira paimfa ndi kukwera kumwamba kwa Yesu Kristu mpaka kumapeto kwa zaka za zana loyamba kumene mabuku ndi makalata a CHIPANGANO CHATSOPANO adalembedwa m'chinenedwe chachi Greek cha nthawi imeneyo.

Mose anamwalira pafupifupi 1400 BC, motero titha kunena kuti Baibulo linapangidwa zaka zoposa 1500.

# Kukwanilitsidwa ndi Kutsiriza

**Koyambilira kwenikweni, akhristu oyamba adadziwa kudzera mwa kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera ndi mabuku omwe ndi a mu Bayibulo ndi omwe sanali. Iwo anali ndi njira zomveka zovomerezera bukulo motero amatha kusiyanitsa bwino lomwe mabuku omwe anali owona (ovomerezeka), komanso omwe sanali owona (apocryphal).**

Martin Luther adaweruza **mabuku osasankhidwawa,** ponena kuti "sawerengedwa kuti ndiogwirizana ndi malemba opatulika." Mukamawerenga malembawa, muwona kuti ndizosemphana kwambiri ndi mabuku a m'Baibulo.

Nkhani zopeka zonena za Ambuye Yesu ndi za atumwi, m'makalata okopedwa ochokera kwa anthu a m'Baibulo komanso mbiri ndi malo zolakwika zingathe kupezeka. Mu 1545, nthawi ya Khonsolo (Msonkhano) ya Trent, mabukuwa adanenedwa kuti ndi "ofanana" ndi mabuku ena a m'Baibuloli, pakati pazinthu zina kuti azithandizira ziphunzitso zophatikiza za Khonsolo. Izi zikuwonetseratu kuti mabukuwa (Apocrypha) alibe chiyambi cha umulungu. Ndiye chifukwa chake muyenera kuwerenga zolemba za Baibulo popanda mabuku owonjezera.

**Mawu a Mulungu adaphatikiza mitundu yosiyanasiyana ya mabuku omwe adasankhidwa mosamala kutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera, ndipo adamaliza kwanthawi yonse.**

**Baibulo imatchedwa kuti Buku Lopatulika, chifukwa linachokera kwa Mulungu, osati ku ulamuliro wa anthu. Ngakhale lero lino lili ndi ulamuliro wapamwamba kwambiri pa chikhulupiriro chathu komanso moyo wathu.**

**Thambo ndi dziko lapansi zidzapita, koma mawu anga sadzachoka ayi.**
Baibulo – Mateyu 24:35

# Zolemba Pamanja Zodalirika


**Nyumba ya amonke ya Saint Catherine m'mapiri a Sinayi. Munali mkati mwa zaka za m'ma 1900 pomwe Tischendorf anapeza Codex Sinaiticus.**

Zolemba pamanja zoposa 5,000 ndi zidutswa za Chipangano Chatsopano m'chinenero cha chigriki. Mpukutu wodziwika kwambiri ndi Codex Sinaiticus, ukadali pafupifupi Baibulo lokwana linasungidwa kwathunthu m'Chigiriki **kuyambira m'zaka za m'ma 300** lomwe lidapezedwa ndi wophunzira Constantine von Tischendorf ku Monastery ya Saint Catherine pa Kinenula ya Sinai mu 1859.Chuma cha zolemba za Baibulo zopanda mtengo sizinangokhala ndi mbali za Chipangano cha kale, komanso Chipangano Chatsopano chonse **ndi mabuku ake 27.**

Kuwonjezera pa zolemba pamanja ndi zidutswa zosiyanasiyana za Chipangano Chatsopano, panali matanthawuzilidwe akale **pafupifupi 9,000 matanthawuzilidwe akale** kuchokera m'mipukutu yoyambirira. Pamodzi ndi malemba **36,000 a M'baibulo** ochokera mu omwe amatchedwa Abambo a Tchalitchi, zidapangitsa kuti zikonzedwenso kwathunthu za zolembedwa zoyambilira kudzera mukupezanso kwa kathithi.

Palibe mawu amodzi omwe amatsutsa choonadi cha uthenga wa Mulungu mu Chipangano Chatsopano.

**Kulondola kwa kumasulira kwa zolemba za Baibulo kuzaka zonsezo ndi zapadera.**

# Mapanga a Qumran

M'nyengo ya pakati pozizira ndi kutentha ya 1947, mnyamata wochokera ku fuko la Bedouin, yemwe akuti amafuna mbuzi yothawa, adapeza khomo la phanga lobisika kumapiri a Qumran kumadzulo kwa Nyanja Yakufa.

Iye anaponyera mwala pakamwa papang'ono pa phangalo. Anadabwa kwambiri atamva phokoso lakusweka kwa dothi. Ankadzifunsa kuti kodi chimenecho chingakhale chiyani.

Mwakufunitsitsa, adadziponyera m'phanga lodabwitsa ili ndikupeza mbiya zingapo zadongo momwe mudali mipukutu ya zikopa (zolembedwa), zokutidwa ndi chinsalu. Iyi inali mipukutu yakale, yamtengo wapatali kwambiri yomwe idakalipobe yabwino modabwitsa, ngakhale zatha zaka 1,900.

M'busa wachinyamatayo adatenga mpukutu ndipo adadabwa kuti akatswiri ofukula za m'mabwinja amawakonda. Kusaka mipukutu yapaderayi kunabuka pakati pa adyera ndi akatswiri ophunzira.

Mitengo ya mipukutuyi inakwera kukhala mamiliyoni. Kupeza kopangitsa chidwi uku m'maphanga a Qumran kunapangitsa kuti akatswiri asukulu za padziko lapansi ayambe kusangalala.

Kwa ife, mpukutu wa buku la Yesaya ndiwofunikira koposa monga momwe lili lathunthu lakale kale kwambiri la buku la m'Baibulo.

Palibe kukayikira m'kumodzi komwe kumatsimikizirika zolemba pamanja, zomwe zidalembedwa m'ma 2000 BC. Poyerekeza ndi buku laling'ono la Amasorete a zaka chikwi chimodzi (buku lachihebri Baibulo la Chihebri) la buku la Yesaya, ophunzirawo adapeza modabwitsa kuti palibe kusiyana kulikonse! Malembawo adalumikizana lina ndi linzake momveka bwino!







Chifukwa zolemba za mpukutuwu sizinasinthidwe, otsutsa onse a Baibulo omwe ananena kuti buku la Yesaya linalembedwa zaka zambiri zapitazo ndipo silinali lolondola sanatsimikiziridwe.

Zina mwazomwe anapeza ku Qumran zinali mipukutu pafupifupi 250 ya zolembedwa zakale za Baibulo za Chipangano Chakale zomwe zimatsimikizira kuti zolembedwa pamanja zidalembedwa molondola kwambiri.

**Mulungu amawayang'anira Mawu Ake kuti tithe kuwagwira iwo m'manja mwathu osasinthidwa. Mawu a Mulungu ali ngati thanthwe: sungawasunthe.**

**Koma mawu a Mulungu akhala kosatha.**

**Baibo – 1 Petro 1:25**

# Kupanga Baibulo
## << Kale ndi Tsopano >>



Zaka zopitilira 500 zapitazo chitukuko chosindikiza chidasintha dziko. Izi zisanachitike, ngati munthu akufuna kuti akhale ndi Baibulo zimayenera kuti zizilembedwa pamanja, zomwe zimawononga nthawi yambiri motero zimawononga ndalama zambiri.

Kuti tisunge zomwe zinali zoyambirira, zinali zoyenera kudziwa zolemba pamanja zakale kwambiri chifukwa kukopera kuchokera kumodzi kupita kwina kumabweretsa kuyipa kosinthidwa.





Kupeza zolembedwa kumatsimikizira zinthu zododometsa: zolemba zakale za 3,000+ zodziwika bwino za Chihebri zimagwirizana modabwitsa, china ndi chinzake, ndikutsimikizira zolembedwa zodziwika. Zigawo zakale kwambiri za Baibulo, zomwe zinakhala m'zaka pafupifupi 3,500 zapitazo, zaperekedwa ndendende munthawi yathu ino.



Kodi zinatheka bwanji? Pakulemekeza Mawu Opatulika a Mulungu, Ayuda adatsata malamulo ambiri kuti athe kukopera molondola. Mwachitsanzo, Chilembo chimodzi kapena kupezeka kwa mawu ena zidawerengedwa ndikuonedwa mobwereza bwereza.

Masiku ano, matembenuzidwe ambiri a Mabaibulo akhoza kupangidwa mowumira chuma komanso munthawi yaying'ono kudzera m'nyumba zamakono zosindikiza mabuku.

Pakadali pano, ma Baibulo ambiri a digito pa intaneti ndi mapulogalamu a Baibulo alipo a ulele.



**Koma mawu a Mulungu anakula ndi kuchuluka.**

Baibulo – Machitidwe 12:24

# Baibulo ndi Sayansi

Kodi zingatheke bwanji kuti buku lomwe lidalembedwa kalekale chonchi ndi zonena zake pazachilengedwe ndi mbiri lizikhala lolondola nthawi zonse? Kodi nchifukwa ninji sikuli kotheka mwasayansi kutsutsa Baibulo? Pali zitsanzo zambiri pomwe sayansi yamakono yatenga nthawi yayitali kuti aphunzire zomwe Baibulo limanena. Nazi ziwiri mwa izo:

## Kodi dziko lapansi ndi lozungulira?



Mulungu sananenepo kuti dziko lapansi linali chimbale komanso kuti dzuwa limazungulira dziko lapansi. Izi ndi zomwe asayansi ambiri akhala akukhulupirira kwa nthawi yayitali.

M'malo mwake, Mulungu akuti mu limodzi la mabuku akale kwambiri a m'Baibulo, mu Yobu 26:7: **"Ayala kumpoto popanda kanthu; nalenjeka dziko pachabe."**

## Kodi kalulu ndi Nyama yobzikula?



Mu Levitiko 11:4 & 6 akuti: **"Koma, izi zokha simuyenera kuzidya mwa zobzikula ... Kalulu, popeza abzikula koma..."**

Mfundo ya Kalulu kukhala ruminanti idanenedwa ngati yabodza kwazaka zambiri.

Komabe, m'zaka za zana la 19 asayansi adazindikira kuti kalulu ali ndi mitundu iwiri yosiyanasiyana yotulukira. Umodzi mwa iyo amadyanso kachiwiri kuti ayamwe michere yofunika.



Chifukwa chake sayansi ikukakamizidwa kuvomerezana ndi Baibulo mobwereza bwereza patatha zaka zakafukufuku. Komanso, zonena za m'Bayibulo sizikutsutsana ndi zowona zamakono za sayansi komanso akatswiri ofukula zinthu zakale.





## Kodi pangakhale kusiyananso?

**Kodi Mulungu, yemwe adalenga chilengedwe chonse ndi kutipatsa Mawu Ake (Bayibulo), azidzitsutsa Iye mwini? Ayi, zonsezi ndi mavumbulutso a Mulungu, CHILENGEDWE ndi MAWU, zonse zimatsimikizirana china ndi chinzake.**

# Uthenga wa Bayibulo

## > Mulungu adakulengani

**Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake; m'chifanizo cha Mulungu adamlenga iye; wamwamuna ndi mkazi Iye adawalenga.** **Baibulo – Genesis 1:27**

Ndinu cholengedwa cha Mulungu. Pali m'modzi yekha wa inu padziko lapansili. Kuphatikiza pa izi, thupi lanu ndi ntchito zake zonse – ubongo, machitidwe, ziwalo – zidapangidwa bwino kwambiri ndi Mulungu. Palibe lingaliro la nthawi ndi mwayi – monga lingaliro losatsimikizika la chisinthiko likunena. Mulungu adalenga munthu "m'chifanizo Chake", i.e. kumuyimira Iye m'chilengedwechi.

**Komabe, munthu adachimwa ndipo adapatuka kwa Mulungu.**

## > Mulungu anakuyikani inunso, monga "wochimwa"

**Pakuti palibe kusiyana; pakuti onse adachimwa, naperewera pa ulemerero wa Mulungu.** **Baibulo – Aroma 3:22 & 23**

Kuchimwa kumatanthauza kuchita zinthu popanda kugonjera Mulungu. Sizikupanga kusiyana kulikonse ngati chimo likuwoneka ngati chochitidwa, kapena ngati chikunenedwa mokweza, kapena mwina kuchitidwa mu malingaliro. Ambuye Yesu nthawi ina ananena kuti kudana ndi munthu ndi tchimo lalikulu ngati kupha!

## > Mulungu adzakhala woweruza wanu

**Ndipo popeza kwaikikatu kwa munthu kufa kamodzi, ndipo atafa chiweruziro ...** **Baibulo – Ahebri 9:27**

Mulungu ndi Woyera ndi wachilungamo. Ichi ndi chifukwa chake tsiku lina ayenera kuweruza zonse zomwe sizigwirizana ndi chilengedwe Chake. Baibulo limafotokoza momveka bwino kuti munthu aliyense amene wamwalira popanda kukhululukidwa machimo ayenera kuyembekezera kulekanitsidwa ndi Mulungu kwamuyaya. Mosiyana ndi kumwamba komwe aliyense amene ali ndi ubale ndi Ambuye Yesu adzakhale, padzakhala malo omwe Baibulo limawatcha "gehena" kapena "nyanja yamoto". Mulungu sadzakhalako, ndipo sipadzakhala kuthekera kolumikizana ndi Iye.

**Komabe pali chiyembekezo!**

## > Mulungu ali ndi chidwi chachikulu mwa inu

**Umo chikondi cha Mulungu chidawonekera kwa ife, kuti Mulungu watumiza Mwana wake wobadwa yekha kudziko lapansi, kuti tikhale ndi moyo kudzera mwa Iye.** **Baibulo – 1 Yohane 4:9**

Yang'anani pamtanda wa Kalvari pomwe Yesu khristu adakumana ndi chilango chochokera kwa Mulungu mwa kuzunzika m'zowawa zoopsa. Anasiyidwa ndi Mulungu pamtanda chifukwa Iye ananyamula machimo athu. Sitingathe kudziwa m'mene izi zinakhalira kwa Ambuye Yesu, yemwe anali wopanda tchimo.

**Kodi mukuwona m'mene Mulungu amakukonderani?**

# Chithandizo cha Mulungu + Njira ya chipulumutso

Tili olekanitsidwa ndi Mulungu kudzera muuchimo. Mulungu sangavomere kuyesetsa kwathu kuti tidzikonze tokha. Mulungu, m'chiyero ndi kuyera kwake, ayenera kuweruza zoipa. Pali njira imodzi yokhayo yotulukira: tikuyenera kuvomereza njira ya chipulumutso yomwe imachokera kwa Mulungu Mwini.

> **Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.** **Baibulo – Yohane 3:16**

Pofuna kuwululira Mulungu, Mlengi wanu, Yesu khristu adakhala munthu ndipo adabwera kudziko lapansi kwa ife.

Yesu Khristu watiwonetsa ife chikondi cha Mulungu. Anatsimikizira ichi mokwanira mwa kukuferani pamtanda wa Kalvare. Monga wokuyimirani, Iye adadzitengera Yekha chilango cha machimo anu – ngati mumukhulupirira Iye.

**Ngati mungavomereze izi mwachikhulupiriro ndikuwululira machimo anu kwa Mulungu, adzakupatsani chikhululukiro ndi moyo wosatha.**



> **Ngati tivomereza machimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chilichonse.** **Baibulo – 1 Yohane 1:9**

Yesu Kristu ali moyo! Adawuka kwa akufa ndi kubwelera ku mwamba.

Uthenga wabwino uwu wakhala ukulalikidwa kwa zaka pafupifupi 2000. Chipulumutso chikhoza kuperekedwa kwa anthu onse. Aliyense amene akhulupirira mwa Yesu Khristu – m'modzi yekhayo Mpulumutsi – adzamasulidwa ku chiweruziro chamuyaya cha Mulungu. Aliyense amene avomereza ntchito ya chiwombolo ya Yesu Khristu mchikhulupiriro adzayesedwa olungama pamaso pa Mulungu.

> **... Kuyesedwa olungama kwaulere ndi chisomo chake, mwa chiombolo cha mwa Khristu Yesu.** **Baibulo – Aroma 3:24**



# Malonjezo Aumulungu

Ku ziphatikiza, kalata ya umulungu, Baibulo, likuti:

**1. Mulungu ndi woyera**

> *Ayenera kuweruza ndikulanga tchimo!*

**2. Mulungu ndi chikondi**

> *Akufuna kukukhu-lulukirani machimo anu onse.*

Mulungu akhoza kukukhululukirani machimo anu chifukwa Mwana wake, Yesu Khristu, wadzitengera Iye yekha chilango cha uchimo ndikukwaniritsa chili chonse chofunidwa ndi Mulungu Woyera.

Komabe, kuti mukhululukidwe nokha muyenera kubwera pamaso pa Mulungu m'kulapa machimo anu, ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu adafera pamtanda, ngakhale chifukwa cha inuyo, monga Mpulumutsi ndi Muomboli.

**Kenako Mulungu ali ndi malingaliro opitilira 1,000 osasinthika, a umulungu omwe ali okonzeka m'Mawu ake, Bayibulo.**

**Mupeza mfundo zochepa izi pano >>>**

**Iye amene akhulupirira Mwanayo ali nawo moyo wosatha; ndipo iye amene sakhulupirira Mwanayo sadzawona moyo, koma mkwiyo wa Mulungu ukhala pa iye.**

Baibulo – Yohane 3:36

**Iye amene amva mawu anga ndikukhulupirira Iye amene ananditumа Ine ali nawo moyo wosatha, ndipo salowa mkuweruza, koma wachoka ku imfa nalowa m'moyo.**

Baibo – Yohane 5:24

**Koma onse amene anamulandira Iye, kwa iwo anawapatsa mphamvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu akhulupirira dzina Lake.**

Baibulo – Yohane 1:12

**Usawope, chifukwa ndakuwombola iwe; Ndakutchula dzina lako; iwe uli wanga.**

Baibulo – Yesaya 43:1

# Mwana Wolowerera

## Nkhani yochokera m'Baibulo

Ndipo Iye adati, Munthu wina adali ndi ana amuna awiri: Ndipo wam'ng'onoyo adati kwa atate wake, "Atate, ndigawirenitu zanga za pa chuma chanu". Ndipo iye adamugawira za moyo wake. Ndipo pakupita masiku wowerengeka mwana wam'ng'ono adasonkhanitsa zonse, napita ulendo wake ku dziko lakutali; ndipo komweko adamwaza chuma chake ndi makhalidwe a chitayiko. Ndipo pamene adatha zake zonse, padakhala njala yayikulu m'dziko muja, ndipo iye adayambakusowa. Ndipo adapita nadziphatikiza kwa mfulu imodzi yadziko lija; ndipo uyu adamtumiza kubusa kwake kukaweta nkhumba. Ndipo adalakalaka kukhutitsa mimba yake ndi makoko amene nkhumba zimadya, ndipo palibe munthu adam'ninkha kanthu. Koma pamene adakumbukira mumtima, adati, "Antchito wolipidwa ambiri wa atate wanga, ali nacho chakudya chochuluka, ndipo ine ndiwonongeke kuno ndi njala! Ndidzanyamuka ndipite kwa atate wanga, ndipo ndidzanena naye, Atate, ndidachimwira kumwamba ndi pamaso panu. Ndipo sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu. Mundiyese ine ngati m'modzi wa antchito anu." Ndipo iye adanyamuka, nadza kwa atate wake, koma pakudza iye kutali, atate wake adamuwona, nagwidwa chifundo, nathamanga, namkupatira pakhosi pake, nampsopsonetsa. Ndipo mwanayo adati kwa iye, "Atate ndidachimwira kumwamba ndi pamaso panu, sindiyeneranso konse kutchulidwa mwana wanu." Koma atateyo adati kwa atumiki ake, Tulutsani msanga mwinjiro wokometsetsa, nimumbveke; ndipo mpatseni mphete ku dzanja lake ndi nsapato ku mapazi ake; Ndipo idzani naye mwana wa ng'ombe wonenepa, mumuphe, ndipo tidye, tisekere. "Chifukwa mwana wanga uyu adali wokufa, ndipo tsopano wakhalanso ndi moyo; anali wotayika ndipo wapezeka." Ndipo adayamba kusekera Koma mwana wake wamkulu adali kumunda. Ndipo pakubwera iye ndi kuyandikira kunyumba, adamva kuyimba ndi kubvina. Ndipo iye adayitana m'modzi wa mtumiki, namfunsa, zinthu izi nzotani? Ndipo iye adati kwa iye, M'ng'ono wako wafika; ndipo atate wako adapha mwana wa ng'ombe wonenepa, chifukwa adamlandira iye wamoyo. Koma iye adakwiya ndipo sadafuna kulowanso. Ndipo atate wake adatuluka namdandaulira. Koma iye adayankha nati kwa atate wake, Onani, ine ndidakhala mtumiki wanu zaka zambiri zotere, ndipo sindidalakwira lamulo lanu nthawi ili yonse; ndipo simunandipatsa ine kamodzi konse mwana wa mbuzi, kuti ndisekere ndi abwenzi anga. Koma pamene anadza mwana wanu uyu, wakutha za moyo zanu ndi akazi achiwerewere, mudamphera iye mwana wa ng'ombe wonenepa. Koma iye adanena naye, "Mwana wanga, iwe uli ndi ine nthawi zonse, ndipo zanga zonse ziri zako. Koma kudayenera kuti tisangalale ndi kukondwera: chifukwa m'ng'ono wako uyu adali wakufa ndipo ali ndi moyo; adatayika, ndipo wapezeka."

Baibulo – Luka 15:11-32




# Zipembedzo Zambiri – Zonse Mulungu Yemweyo?

Ndi lingaliro lofala padziko lonse lapansi kuti zipembedzo zonse zimatsogolera kwa Mulungu m'modzi, kudzera munjira zosiyanasiyana.

Izi zikutsutsana kwathunthu ndi uthenga wa Baibulo kuchokera mkamwa mwa Yesu Khristu: "Ine ndine njira, ndi chowonadi ndi moyo. Palibe munthu amafika kwa Atate osadzera mwa Ine" (Yohane 14:6). Choonadi ichi chimakanidwa masiku ano.

Mwachitsanzo, kuyerekezera Korani ndi Baibulo kumawonetsa kuti "Allah wochokera ku Chisilamu" sangakhale Mulungu wa m'Baibulo:

**KORANI**

... Chifukwa chake khulupirirani Alla ndi amithenga ake, ndipo musanene: "Atatu" ... Allah ndi Mulungu m'modzi. Iye ndi Wokwezeka kwambiri Iye ali pamwamba ndi mwana.
Korani – kutengedwa kuchokera mu Surah 4

**BAIBULO**

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.** Baibulo – Yohane 3:16



**KORANI**

Ndi kunena kwawo, "Inde, tapha Mesiya, Yesu mwana wa Mariya, mthenga wa Mulungu." Ndipo iwo sanamuphe iye, kapena kumupachika; koma wina adazifanizira iye kwa iwo.
Korani – kutengedwa kuchokera mu Surah 4

**BAIBULO**

**Pakuti uthenga wa mtanda ndiopusa kwa iwo amene akuwonongeka, koma kwa ife amene tikupulumutsidwa ndi mphamvu ya Mulungu... koma ife timalalikirira Yesu wopachikidwa, kwa Ayuda chopunthwitsa ndi kwa amitundu chinthu chopusa.**
Baibulo – 1 Akorinto 1:18 & 23

Korani imakana momveka bwino kuti "Allah" ali ndi mwana wamwamuna, utatu wa Mulungu komanso kuti Yesu Kristu adafera pamtanda! Koma Mulungu wa m'Baibulo ndi Mulungu wamoyo. Kuchokera m'chikondi cha kwa inu ndi ine, Iye adapereka Mwana wake ngati nsembe ya machimo – mwa kuti Khristu adazunzika ndi chiweruzo cha Mulungu ndikulowa muimfa. Ichi ndi chifukwa chake "Allah" sangakhale Mulungu wa m'Baibulo, ndiye Atate wa Ambuye Yesu Khristu.

## Mwachidule: Chikhristu cha m'baibulo sichipembedzo ayi!

**Muzipembedzo zosiyanasiyana zadziko lapansi, munthu amayesera kupeza njira yopita kwa Mulungu kudzera mu kuyesayesa kwake.**

**Koma Baibulo limatiwonetsa Mulungu Woyera amene adadzera kwa ife mwa Mwana wake Yesu Khristu, kuti aliyense wokhulupirira Iye ndi kuvomereza machimo ake kwa Iye adzapulumutsidwa.**

**Koma kwa iye amene sagwira ntchito koma akhulupirira Iye amene alungamitsa osapembedza, chikhulupiriro chake chimayesedwa chilungamo.** Baibulo – Aroma 4:5

# Onani M'tsogolo



Baibulo limatipatsa malonjezo odalirika am'tsogolo.

Tazunguliridwa ndi nkhawa ndi zisoni masiku ano: Imfa, chiwerewere, chiwawa, njala, nkhondo, matsoka achilengedwe, mavuto azachuma, matsoka, uchifwamba...!

Komabe, Yesu Kristu abweranso posachedwa! Mulungu amatiuza momveka bwino mu Baibulo kuti masiku akatsala pang'ono pakubwera kwake adzadziwika ndi zochitika ngati izi. Wowerenga Baibulo amadziwanso momwe zinthu zidzakhalire:

Mulungu adzaweruza dziko lapansi, lomwe linapatuka kwa Iye ndipo tsopano likumira m'machimo. Komabe Mulungu **"tsopano akulamula anthu onse ponseponse kuti alape, chifukwa adakhazikitsa tsiku lomwe adzaweruza dziko lapansi ..."** (Machitidwe 17:30 & 31).

Izi zidzachitika kudzera mwa Mwana wake Yesu Khristu, yemwe posachedwapa adzabweranso kuchokera kumwamba kudzaweruza. Iye, wonyozekayo ndi wopachikidwa, adzabweranso monga wogonjetsa ndi ulamuliro wa oweruza wamkulu: Iye ndiye amene **"anasankhidwa ndi Mulungu kukhala Woweruza wa amoyo ndi akufa"** (Machitidwe 10:42).

**Chiweruziro ndichotsimikizika – koma pali chiyembekezo kwa inu!**



Baibulo linaneneratu mwatsatanetsatane za kubadwa kwa Yesu Kristu komanso imfa yake ndi kuukitsidwa kwake zaka zambiri izi zisanachitike. Monga momwe Yesu Kristu adapereka moyo wake chifukwa cha inu, Mulungu amakupatsirani chisomo chake ndi chikhululukiro Chake ngakhale lero.

**Bwerani lero, atero Mulungu – mwina lingakhale lochedwa kwambiri mawa:**

**Onani, ino ndiyo nthawi yolandiridwa; tawonan itsopano, ndilo tsiku la chipulumutso.** Baibulo – 2 Akorinto 6:2

Landirani zomwe Mulungu wakupatsani, kenako mudzalandira chipulumutso chamuyaya kuchokera kuchiweruziro cha umulungu. Kuti muchite izi, muyenera kubwera kwa Iye pakubvomereza machimo anu. Mulungu Wamphamvuyonse amalosera motsimikiza; palibe munthu amene angachite ichi. Maulosi mazana angapo a m'Baibulo akwaniritsidwa motsimikiza. Baibulo linaneneratu za: maufumu mazana ambiri kale; kubadwa kwa Yesu Kristu kusanafike; kuwonongedwa kwa Yerusalemu mu 70 AD; kubalalitsidwa kwa Ayuda padziko lonse lapansi ndi zina zotero.

**Zonsezi zimatsimikizira mwanjira yapadera kuti Baibulo ndi Mawu a Mulungu.**

Mwachitsanzo, Baibulo limakamba za Ayuda (anthu a Israeli) pa Deuteronomo 28:64 & 65: **"Ndipo Yehova adzakubalalitsani mwa mitundu yonse, kuyambira malekezero a dziko lapansi kufikira kumalekezero ena.... Ndipo mwa a mitundu simudzapumula, inde sipadzkhala popumulira phazi lanu."**

**>> Dziweruzireni nokha ngati izi zidakwaniritsidwa kapena ayi!**

# Moyo ndi Waufupi

## ndipo umadutsa ngati Kanema

**Lero** muyenera kudzikonzekeretsa nokha kukumana ndi Mulungu. Kodi mukufuna kupitilizabe kutembenukira kwa Mulungu? Kenako kudzakhala kochedwa kwambiri kwa inu tsiku lina!

























**Chifukwa chake:**

*Yanjanitsidwani ndi Mulungu.*

**Baibulo – 2 Akorinto 5:20**





# Ndemanga zochititsa Chidwi Zokhudza Baibulo

"Ndidaphunzira mosamalitsa m'Malemba opatulika kwa zaka 40, ndipo chikhulupiriro changa chalimba kwambiri kuposa zaka 40 zapitazo. Malonjezo onse ndi odalirika komanso owona."

Hudson Taylor (1832-1905), Wamishoni ku China

"Ndawerenga Malemba opatulika pafupipafupi komanso mozama, ndipo ndikuganiza kuti buku lakaleli ... lili ndi mphamvu zambiri ndi kukongola mu chilankhulo kuposa mabuku ena aliwonse, kaya la zaka kapena Chilankhulidwe chomwe adalilemba."

Sir William Jones (1746-1794), m'modzi mwa anthu aluso kwambiri mwa zilankhulo (zilankhulo 28) komanso waluso ku m'mawa

"Osauka bwanji, ndi onyozeka bwanji mawu a anzeru ndi zotsutsana zawo zonse poyerekeza ndi Baibulo. Kodi zingatheke kuti buku, lomwe ndi losavuta komanso nthawi yomweyo lokwanira, lingakhale lofanana ndi mawu a anthu? "

Jean Jacques Rousseau (1712-1778), wafilosofi



"Baibulo ndi zonse chikalata chapadera komanso buku lodalirika loyambira la mbiri. Latsogolera kupeza miyandamiyanda ya zofufuza zinthu zakale, ndipo lapanga zowelenga zambiri pa chikhalidwe chakale. Baibulo lakhala likuwonetsa kuti ndilowona kulikonse komwe lingatsimikiziridwe, pakufotokoza tsatanetsatane wochepa komanso mukufotokozera zochitika zazikulu. "

Dave Balsinger ndi Charles E. Seller, akatswiri ofukula za m'mabwinja aku America

"Mu Baibulo mutha kupeza zowonadi zambiri zomwe sizimangopita mu malingaliro athu aumunthu, ndikutiwonetsa momwe kulingalira kwathu kuli kosakwanira. Komabe, m'mawu ake akuluakulu ofunikira, Baibulo silovuta kulimvetsa. "

Charles H. Spurgeon (1834-1892), mlaliki wotsitsimutsa

"Baibulo ndiye chikalata cokhacho cha uthenga wochokera kwa Mulungu chomwe tilinacho chosindikizidwa mu chilankhulo cha anthu. Ichi ndi chifukwa chake Baibulo ndi lapadera komanso lodalirika pamfundo zake zonse. Si sayansi, nzeru kapena malingaliro omwe amakwaniritsa kuwongolera Baibulo. Komabe, m'malo mwake, Baibulo lili ndikuthekera koyeretsa malingaliro athu. "

Prof. Werner Gitt, wamkulu wa kale ku zamauthenga ku PTB dipatimenti Braunschweig

**Ndikosavuta kutsutsa kuti Baibulo ndi lolondola, koma ndi chinthu chosiyana kwambiri ndi kutsimikizira izi.**

# Kutanthauzira kuchokera Kumalemba Oyambirira

Kutanthauzira Baibulo ndi ntchito yovuta. Zolemba zonse za Chiheberi za Chipangano Chakale ndi zolemba za Chigriki za Chipangano Chatsopano zili ndi zilembo zazikulu zokha, zomwe onse zimakhala moyandikana kwambiri opanda mpumilo kapena mpatuliro. Ndi chifukwa chake ndi ntchito yovuta kuti akatswiri azilankhulidwe azindikire pamene pakuyambira chiganizo chatsopano.

Kuphatikiza apo, palibe mavawelo mu chiheberi, monga a, e, i, o, u, koma makonsonanti okha (b, k, t etc.).

Muyenera kuwonjezera mavawelo nokha. Genesis 1:1 kwa ife titha kuwona ngati motere:

PCHYMBMLNGDLNGKMWMBNDDZKLPNS

Kodi mungazindikire chiganizo chotsatirachi: "Pa chiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi"? Choncho tikhoza kuthokoza kwambiri akatswiri omwe amafufuza malembedwe akale awa, nawapeza nawamasulira.

Baibulo loyamba mu chilankhulidwe cha Chichewa lidasindikizidwa mu 1922. Lidatanthawuzilidwa ndi Amishoni ka Dutch Reformed Church ndi Church of Scotland Mission mothandizidwa ndi a Malawi ena. Ntchito imeneyi idachitikira pamalo otchedwa Kaso, Mvera m'boma la Dowa m'chigawo chapakati cha Dziko la Malawi, ndipo lidasindikizidwa ndi a Bible Society of Scotland.





Kukonzanso kunachitika mu 1936 ndi 1966 kuyikamonso mavesi olozera (Mariferensi) ndi magawo ake. Buku lakale kaleli limadziwika kuti Buku Lopatulika ndilo Mawu a Mulungu.

Kuyambira 1952 mpaka lero matembenuzidwe ambiri akhala akuchitika m'zilankhulo zina zolankhulidwa m'Malawi monga; Chitumbuka, Chitonga, Chingonde, Chisena, Chiyao, Chilhomwe komanso matanthawuzilidwe ena a Chichewa.

Pakadali pano, Baibulo kapena mbali zina za Baibulo zikupezeka m'zilankhulo zoposa 3,500. Pafupifupi 97% ya anthu padziko lapansi ali ndi mwayi wowerenga Mawu a Mulungu. Komabe pali omasulira omwe akumasulirabe Baibulo modzipereka m'zilankhulo zambiri kumadera akutali kwambiri padziko lapansi. Nthawi zambiri, izi zimakhala zovuta kwambiri popeza amayenera poyamba kupanga chinenero cholembedwa.

**Baibulo lakhala buku lodziwika bwino ndiponso buku lofalitsidwa kwambiri mu m'dziko la zowerenga. Chiwerengero cha zotanthawuzira (nthawi zina mbali) m'zilankhulidwe zina chakula kwambiri pazaka mazana awiri zapitazi.**

| | |
|---|---|
| Pofika chaka cha 1800, | kutanthawuzila m'zinenelo 75 kunapangidwa. |
| Podzafika chaka cha 1900, | panali matanthawuziridwe 567. |
| Podzafika chaka cha 1953, | panali 1167. |
| Pofika chaka cha 1978, | chiwerengerochi chinali chitakwera mpaka 1600. |
| Podzafika chaka cha 2023, | Baibulo (kapena mbali zake) linali linatanthawuziridwa m'zilankhulidwe pafupifupi 3,600! |

# Buku la Anthu Onse

**> lolemba ndi anthu 40**
**> lotanthauziridwa ndi mazana,**
**> kusindikizidwa ndi zikwizikwi,**
**> lowerengedwa ndi mamiliyoni.**

Palibe buku lina lililonse lomwe linafalitsidwira m'zilankhulidwe ndi zikhalidwe zambiri monga Baibulo. Ndi buku lowerengedwa kwambiri padziko lonse lapansi.

Pamasamba atatu otsatirawa, vesi la m'Baibulo kuchokera pa Yohane 3:16 likhoza kuwerengedwa mzilankhulo zosiyanasiyana.

**Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nawo moyo wosatha.**

Vesi iyi, imatchedwanso "mtima wa Baibulo", imalongosola mwachidule uthenga wabwino wa Mulungu kwa anthu:

**> Mulungu amakukondani kwambiri kotero kuti adapereka Mwana wake chifukwa cha inu.**

**> Kudzera mchikhulupiriro mwa Iye mudzapulumuka.**



**Kikongo** — Congo

**Kadi muna nzola kazolele nza o Nzambi i kavanin'o Mwan'andi amosi, kimana konso on okwikilanga muna yandi ke vila ko, moys a mvu ya mvu kevwa.**

**Heberi** — Israel

כִּי כֹּה אָהַב אֱלֹהִים אֶת הָעוֹלָם עַד כִּי נָתַן אֶת בְּנוֹ יְחִידוֹ
לְמַעַן לֹא יֹאבַד כָּל הַמַּאֲמִין בּוֹ, אֶלָּא יִנְחַל חַיֵּי עוֹלָם.

**Takishi** — Turkey

**Çünkü Tanrı dünyayı o kadar çok sevdi ki, biricik Oğlu'nu verdi. Öyle ki, O'na iman edenlerin hiçbiri mahvolmasın, hepsi sonsuz yaşama kavuşsun.**

**Bengali** — India

কারন ঈশ্বর এই জগতকে এতোই ভালবাসেন, যে, তিনি তার একমাত্র জন্মগ্রহণ পুত্রকে দিলেন যেন যে কেউ সেই পুত্রের উপর বিশ্বাস করে সে বিনষ্ট হয় না বরং অনন্ত জীবন লাভ করে

**Hangariyani** — Hungary

*Úgy szerette Isten a világot, hogy egyszülött Fiát adta, hogy aki hisz őbenne, el ne vesszen, hanem örök élete legyen.*

**Burmese** — Myanmar

ဘုရားသခင်၏သားတော်ကိုယုံကြည်သောသူအပေါင်းတို့သည်ပျက်စီးခြင်းသို့မရောက်ထာဝရအသက်ကို ရစေခြင်းငှါဘုရားသခင်သည်မိမိ၌တပါးတည်းသောသားတော်ကိုစွန့်တော်မူသည်တိုင်အောင် လောကီသားတို့ကိုချစ်တော်မူ၏။

**Tchayinisi** China

神爱世人，甚至将祂的独生子赐给他们，叫一切信祂的，不至灭亡，反得永生。

**Amharic** Ethiopia

**በእርሱ የሚያምን ሁሉ የዘላለም ሕይወት እንዲኖረው እንጂ እንዳይጠፋ እግዚአብሔር አንድያ ልጁን እስኪሰጥ ድረስ ዓለሙን እንዲሁ ወዶአልና።**

**Giriki** Greece

**Επειδή, με τέτοιον τρόπο αγάπησε ο Θεός τον κόσμο, ώστε έδωσε τον Υιό του τον μονογενή, για να μη χαθεί κανένας ο οποίος πιστεύει σ' αυτόν, αλλά να έχει αιώνια ζωή.**

**Arab** Egypt ndi Middle / Near East

لأنَّهُ هكذا أحَبَّ اللهُ العالَمَ حتَّى بَذَلَ ابنَهُ الوَحيدَ، لكَيْ لا يَهلِكَ كُلُّ مَنْ يؤمِنُ بهِ، بل تكونُ لهُ الحياةُ الأبديَّةُ.

**Rashani** Russia

**Ибо так возлюбил Бог мир, что отдал Сына Своего единородного, дабы всякий, верующий в Него, не погиб, но имел жизнь вечную.**



**Chipwitikizi** Portugal

*Porque Deus amou o mundo de tal maneira que deu o seu Filho unigênito, para que todo aquele que nele crê não pereça, mas tenha a vida eterna.*

**Japanizi** Japan

神は、実に、そのひとり子をお与えになったほどに、世を愛された。それは御子を信じる者が、ひとりとして滅びることなく、永遠のいのちを持つためである。

**Telugu** India

**దేవుడు లోకమును ఎంతో ప్రేమించెను. కాగా ఆయన తన అద్వితీయ కుమారునిగా పుట్టిన వానియందు విశ్వాసముంచు ప్రతివాడును నశింపక నిత్య జీవము పొందునట్లు ఆయనను అనుగ్రహించెను.**

**Polishi** Poland

Albowiem tak Bóg umiłował świat, że Syna swego Jednorodzonego dał, aby każdy, kto weń wierzy, nie zginął, ale miał żywot wieczny.

**Jeremani** Germany

**Denn so hat Gott die Welt geliebt, dass er seinen eingeborenen Sohn gab, damit jeder, der an ihn glaubt, nicht verloren gehe, sondern ewiges Leben habe.**

# Mungathe Kuwerenga Baibulo Mu njira Zosiyanasiyana:

- Mungathe kuwerenga **ngati chidutswa cha zowelenga zakale** kuti mukwaniritse chidwi chanu.
- Mungathe kuwerenga **ngati buku la mbiriyakale** kuti mumve zambiri za nthawi zakale.
- Mungathe kuwerenga **mwanzeru kuti** mufufuze bwino ndikuweluza mwazifukwa mfundo zake.
- Komabe, mungathe kuwerenganso Baibulo **mwachikhulupiriro,** monga uthenga wa Mulungu mwachindunji kwa inu lero.

Ngati muwerenga Baibulo ngati uthenga wochokera kwa Mulungu, chikondi cha Mulungu, chomwe mutha kuchiwona mwa Yesu Khristu, chingathe kulankhula ndi mtima wanu. Kenako chikumbumtima chanu chidzaunikilidwadi ndi Mulungu monganso Yesu adawunikira ndi ntchito ndi mawu ake.





ZOPANGATSA CHIDWI

## Baibulo losindikizidwa laling'ono kwambiri

**> Baibulo la thunthu**

Baibulo laling'ono losindikizidwa lomwe lodziwika kwa ife limangokulirapo pang'ono kuposa ndalama ya 2 €. Baibulo ili ndi 2.8cm kutalika, 3.4cm mulifupi ndi 1cm kunenepa ndipo lili ndi masamba 1514. Mutha kuwerenga chilichonse bwino ndi galasi lokulitsa.



## Baibulo laling'ono kwambiri

**> pa digito ya makorotchipi**

Mu 2008, asayansi aku Israeli ochokera ku Institute of Technology ku Haifa adatha kulemba Chipangano Chakale pa theka la millimeter. Mawu opitilira 300,000 a m'Chipangano Chakale m'chilankhulidwe cha chiheberi adasungidwa pa chipangizo cha silicon chip mulingo umodzi ndi kam'bulu ka shuga. Zinali zothandizidwa ndi nanotechnology kuti chonyamulira chotere cha mini-data chipangidwe. Kuti muwerenge malembawo, nkhanizo zimayenera kusinthidwa kenako ndikukulitsidwa kwa nthawi 10,000.

## Kodi zingapitirire kuchepera?

**> DNA – yosungira ya mtsogolo**

Mulungu, mlengi, adabzala njira yabwino kwambiri yosungiramo mthupi la aliyense wa ife. Mphamvu yake yosungira imaposa chilichonse chomwe chikudziwika kwa ife pano: ndi chingwe cha DNA chomwe chili ndi mamilimita zikwi ziwiri. M'kati mwake muli mauthenga ambiri a mtundu wa munthu aliyense. Ngati tili ndi DNA yokonzedweratu yayikulu ngati m'bulu wa shuga yokhala ndi zoyankha zake ku luso lolemba ndi kuwerenga, titha "kusungira" Mabaibulo pafupifupi wani biliyoni pa cimenechi. Asayansi akukhu-lupirira kuti mitundu yayikulu ya DNA ipezeka m'zaka zochepa.

# Yesu – Bwenzi lathu Lopambana



Ana anakopeka ndi Iye. Iye mosangalala adanyamula ana ang'ono m'manja mwake. Anali wamphamvu! Mphepo yamkuntho inawomba mafunde ndi ngalawa imene Iye anakhalamo inali pachiwopsezo chachikulu. Adadzudzula mphepo ndipo nyanja idakhala bata. Anachiritsa odwala ndipo anamvera chisoni anthu onse – osauka komanso olemera. Anaona tchimo m'mitima yawo, gwero la mavuto onse. Komabe mkazi yemwe anali ndi mbiri yoyipa samamuopa Iye. Kulira pa zoyipa zake zomwe, anabwera kwa Iye, ndipo adamkhululukira machimo ake onse. Tsiku lina adamutenga Iye kapolo! Adasankha kuti apite. Anali wabwino komanso wangwiro – ndipo motero Iye sanafanane ndi moyo wawo wochimwa. Chifukwa chake, adaganiza kuti amuchotsere Iye.

**Iye anakhomedwa pamtanda kuti afe.**

Koma sanadziwe kuti Iye anadziwiratu izi zisanachitike! Iye, Mwana wa Mulungu, anabwera kuchokera kumwamba kudzafa. Anafuna kutipulumutsa ife kuimfa, imfa yamuyaya.



Koma chimwemwe bwanji! Ambuye Yesu sanakhale m'manda. Anauka m'manda. Alimoyo ndipo ali kumwamba tsopano. Amationa ife ndipo amatimvera chisoni. Iye amakudziwani ndipo amafuna kuti akukhululukireni zolakwa zanu zonse ngati muvomeleza machimo anu ndi kuwulula kwa iye, monga mkazi amene tamutchula uja.

"Inde" ndi zomwe adzanene kenako, "Ndingathe kukukhululukira iwe machimo ako tsopano chifukwa Ine ndinalandira chilango chake pa mtanda."

**Ndipo kenaka nkhani yatsopano iyamba:** nkhani ya moyo wanu watsopano, wosinthika, chifukwa udzakhala wosiyana kwambiri ndi momwe udaliri mpaka pano. Adzakhala bwenzi lanu lapamtima. Mudzatha kukambirana chilichonse ndi Iye (ichi chimatchedwa "kupemphera"). Mukatero mudzafunika kuwerenga Baibulo panokha kuti mumudziwe bwino.

Baibulol lidzakhala buku lochititsa chidwi kwa inu. Mosakayikira mudzafunitsitsa kuwerenga china chake cha Ambuye Yesu tsiku lililonse.

*Iye amangofuna kukhala m'nzanu wapamtima!*





# Kukonza Kwakukulu

Khoma la chipinda cha m'nyamata limawoneka loyipa bwanji! linakutidwa ndi zithunzi zopanda pake ndi zikhwangwani. Tsiku lina amalume ake, ojambula, anabwera kudzacheza. Adali wokwiya powona izi koma sadanene chilichonse.

Patapita masiku angapo pambuyo pake, m'phwake adalandira chithunzi chokongola kuchokera kwa amalume ake. Chojambula ichi chidatenga malo olemekezeka pakhoma la mchipinda chogona, ndipo zithunzi zochepa zidatsitsidwa kuti chikhalepo.

Kuyambira pamenepo, zimawoneka ngati kuti chipinda chosiyana, chowoneka choyera m'chipindachi ndipo pambuyo pake chikwangwani chimodzi chimodzi zimasowa. Sizinayeneranso.

Ngati muyamba kuwerenga Baibulo, zitha kutheka kuti izi ndi izo zidzasowa mukhoma lanu, shelefu lanu la mabuku kapena moyika ma CD. Mwinanso data, masewera kapena kulumikizana pa PC kapena lamya yanu ya makono zichotsedwa. Ndani akudziwa – mwina china chake kuchokera kungodya yamdima mu mtima mwanu chidzasowanso.

**Chifukwa chake, ngati munthu aliyense ali mwa Kristu, ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita; taonani, zakhala zatsopano. iKuwunika kuyanjana bwanji ndi mdima?**

Baibulo – 2 Akorinto 5:17, 6:14

# Buku Lopaatsa chidwi Kwambiri m'dziko lonse Lapansi

"Amayi, musayime, pitilizani kuwerenga! Nkhaniyi ndiyosangalatsa, chonde werengani mpaka kumapeto! "Zoonadi, nkhaniyi ndiyosangalatsa:



**Yosefe, wodedwa ndi abale ake, anaponyedwa mchitsime chopanda madzi, anatulutsidwa pambuyo pake ndikugulitsidwa ngati kapolo ku Egypt, komwe anaponyedwa m'ndende ngakhale kuti anali wosalakwa. Komabe anakhala nduna yayikulu ya ku Aigupto, Iye anapulumutsa banja lake ndi dziko lonselo panthawi ya njala.**

Baibulo – Genesis 37-50

Baibulo lili ndi nkhani zambiri zosangalatsa monga izi zomwe zimapatsa kulingalira ndiponso zimalankhula ku mtima.

Baibulo – Danieli 3

**Tangoganizirani za anzake atatu a Danieli, amene sanafune kugwada pamaso pa fano la mfumu ndipo adaponyedwa mu ng'anjo ya moto chifukwa cha ichi; komabe, adatuluka osavulala.**



**Baibulo ndi buku losangalatsa, ngakhale kwa achinyamata!**

# Kodi Mudadyapo Belladonna?



(Atropa belladonna)

Poizoni wa chomera cha belladonna ndiwowopsa. “Koma ndikufuna kuyesera chifukwa ndikutsimikiza kuti sizindipweteka monga zinapwetekera ena.”

Ngati wina aliyense atalankhula chonchi, ndikoyenera kukayikira kuti ali ndi chiyembekezo. Komabe, kodi nafenso nthawi zina sitimachita chimodzimodzi? Timalowerera kwambiri mu mdziko la zofalitsa ma uthenga (Media), pomwe mfundo za Mulungu zokhudza ukwati ndi banja zimazondotsedwa. Timawerengera mabuku omwe machitidwe a zamatsenga amafotokozeredwa, pomwe mabodza ndi chidwi kukonza zoipa zili malingaliro.

Tikufuna “kuyesa” zinthu izi kuyesera kutsimikizira tokha kuti sitinapwetekedwe nazo. Baibulo imati “tisiye” makutu athu ndi ‘kutseka maso athu’ kuti tisamve kapena kuona zoipa (Yesaya 33:15). Chomcho chidutswa cha upangiri wabwino:

**>>> Osamadya chomela cha Belledonna!**

Ngakhalenso aliyense asalowe m’nyumba mwanu! Pewani chilichonse chosagwirizana ndi malingaliro a Mulungu. Mulungu akufuna kutiteteza ife ku zikoka zoipa ndi njira zoyipa, ndipo adzatero ngati tiwerenga Baibulo. Mawu a Mulungu ndi oyera ndiponso owona, ndi amoyo komanso amuyaya. Amakusonyezani njira yopita ku chisangalalo chenicheni ndi mtendere weniweni.

**Mawu anu ndi nyali ya kumapazi anga ndi kuunika kwa panjira panga.** **Baibulo – Masalimo 119:105**



# Masalimo 23

*>> lemba lodziwika bwino kuchokera mu Bayibulo <<*



**Yehova ndiye m’busa wanga; Sindidzasowa.**

**Andigonetsa ku busa la nsipu: Anditsogolera kumadzi odikha.**

**Atsitsimutsa moyo wanga: Anditsogolera m’mabande achilungamo, chifukwa cha dzina lake.**

**Inde ndingakhale ndiyenda m’chigwa cha mthuzi wa imfa, Sindidzawopa choyipa; pakuti inu muli ndi ine: Chibonga chanu ndi ndodo yanu, izi zindisangalatsa ine.**

**Mundiyalikira gome pamaso panga m’kuwona kwa adani anga: Mwandidzodza mutu wanga ndi mafuta; chikho changa chisefuka.**

**Inde ukoma ndi chifundo zidzanditsata masiku onse amoyo wanga: Ndipo ndidzakhala m’nyumba ya Yehova masiku onse.**

SALIMO LA DAVIDE

**Salimo ili limapita kwa munthu aliyense. Kodi pali china chabwino kuposa kunena kuti: “Ambuye ndiye m’busa wanga?”**

**Munthawi yamavuto, ngakhale pakukumana ndi imfa, munthu angathe kupeza chitonthozo cheni cheni: “Inde, ngakhale ndiyenda m’chigwa cha mthunzi wa imfa ... Inu muli ndi ine.”**

# Chitsimikizo chabwino kwambiri

Pamsika panali wogulitsa zipatso atakhala kumbuyo kwa benchi lake. Mmene kunalibe kunalibe makasitomala, iye amagwiritsa ntchito nthawi iliyonse kuwerenga Baibulo, lomwe linali buku lofunika kwambiri kwa iye.

“Kodi mukuwerenga buku lanji?” **“Baibulo langa, Mawu a Mulungu.”** “Chabwino mukudziwa bwanji kuti awa ndi Mawu a Mulungu? Ndani adakuwuzani? “Mulungu mwini” “oh, Mulungu Iye mwini analankhula kwa inu?” Mbambo adafunsa momnyoza.

Mkaziyo adatayika kwa kanthawi chifukwa samadziwa momwe angatsimikizire **kuti Baibulo ndi Mawu a Mulungu.** Koma kenaka analoza dzuwa lowala ndikunena kwa kasitomala wake kuti: “Kodi mungatsimikizire kuti ili ndi dzuwa?” “kutsimikizira kwa inu?” iye adayankha. **“Ndizosavuta. Chitsimikizo chabwino kwambiri ndichakuti limandipatsa kuwala komanso kutentha.”**

“Ndi momwemo!” Mayiyo anayankha **“Umenewutu ndi umboni wabwino kwambiri kuti bukuli ndi Mawu a Mulungu: limandipatsa kuwala komanso kutentha.”**





# Baibulo lophikidwa

Jan Hus akhoza kutchedwa zonse wokonzanso ndi wofera chikhulupiriro ku Bohemia. Kudzera mu umboni wake, maso a anthu zikwi zikwi adatsegulidwa ku ntchito yathunthu ya chiwombolo kudzera mwa Yesu Khristu.

Koma kufalitsa uku kwa uthenga wabwino sikudakhalitse mdziko limeneli. Jan Hus anawotchedwa pamtengo, mwazi wa akhristu ena unali kuyenda ngati m’mitsinje ndipo kusaka Mabaibulo kunachitika kuti awawononge.



Munthawi imeneyi, mayi, yemwe chuma chake chachikulu kwambiri chinali Mawu a Mulungu, adayimirira kutsogolo kwa uvuni wake kuphika mkate. Mwadzidzidzi anamva kuti amuna aku Khoti Lalikulu la Zigawenga anali akusesa m’mudzimo ndipo akugwira aliyense amene wapezeka ali ndi Baibulo.

Anatenga mwachangu Baibulo lake ndi kukulunga ndi mtanda waukulu, womwe anakauwotchera mu uvuni ndi mikate ina kumbuyo kwake.

Pambuyo pake, nyumba yake idasakidwaso. Chilichonse chinkaponyedwa, kuyambira m’chipinda chapansi pa nyumba mpaka chapamwamba, koma pachabe.

Ozunza atachoka m’nyumbamo, buledi uja anaphika ndipo anachotsa mu uvuni. Ndipo taonani: Baibulo lidazunzika pang’ono monga amuna atatu aja, Sadrake, Mesake ndi Abed-Nego, omwe adaponyedwa m’ng’anjo yoyaka moto. Baibulo imatiuza ife m’mene Mulungu anawatulutsila m’ng’anjo osavulala.

Baibulo – Danieli 3

**O Ambuye Mulungu wanga, ndakhulupilira Inu; mundipulumutse kwa onse ondilonda; nimundilanditse.** Baibulo – Masalimo 7:1



# Diso la Ng'ombe ya mphongo

**“Baibulo si langa”, Pitara adanena kwa m’nzake, “chifukwa mudalembedwa zambiri m’menemu zakuti sindimazimvetsetsa.”**

**Ken adaganiza kwakanthawi. Adadziwa bwino kuti Peter amangofuna kupereka zifukwa. Kungoti dzulo lake anali ataba china chake pabwalo la oyandikana nawo. Choncho Ken adayankha kuti: “Chinthu chimodzi chomwe chidalembedwa m’Baibulo chomwe iwe ungathe kuchimvetsetsa.” “Chabwino, m’chiyani?” “Usabe”**

**Ichi chinali ngati muvi ukubaya mu mtima wa Pitara. Anaganizira za tsiku lapitalo ndipo adachokapo mwakachetechete.**

**Wokhala ndi mtima wachinyengo sapeza zabwino, ndipo wokhala ndi lilime lolakwika amapezeka kuti walakwa.**

Baibo – Miyambo 17:20

# Baibulo lotayidwa

Ndili panjira kunyumba kumapeto kwa sabata, asirikali angapo amayenda limodzi ndikuchita zinthu mosasangalatsa – kusekana komanso nthabwala wina ndi mzake.

Msirikali wachichepere anali atakhala ngodya (pakona) ya chipinda cha sitimayo, akuwerenga Baibulo lake la m’thumba. Mwadzidzidzi, msilikari wina adalumphira, nati: “Tiyeni tisangalale ndi iye.” Atanena izi, iye anakwatula Baibulo m’manja mwake mnyamatayo ndi kuliponya kulitulutsira pawindo.

Izi zonse zidachitika motsatana mumkamphindi, ndipo Baibulo lidagwera pa thilaki. Kodi msirikali wachinyamatayo tsopano adalumphira mokwiya? Ayi, adakumbukira mawu a Ambuye Yesu: **“Ndine wofatsa ndi wodzichepetsa mtima”** (Mateyo 11:29). Anali wachisoni, koma anangokhala chete.

Masabata angapo pambuyo pake, msirikali wachichepereyu adalandira phukusi Bayibulo lake liri mkati. Kalata yomwe inali mkati mwake inali yosangalatsa. Wogwira ntchito za njanji, yemwe anali kugwira ntchito pa thilaki, anali atapeza Baibulo. Pamene adatsegula ndikuyamba kuwerenga, Mulungu adalankhula naye mumtima. Mpaka nthawi imeneyo anali ndi mantha akulu chifukwa cha chikumbumtima cholakwa, koma kudzera mu kuwerenga Baibulo adapeza chikhululukiro cha machimo ake pakukhulupirira ntchito ya chiwombolo ya Ambuye Yesu. Kenako msirikali anamvetsa chifukwa chomwe anakhalira opanda Baibulo lake kwa milungu ingapo. Mulungu ali ndi njira zodabwitsa zofikira mitima ya anthu, ndipo mdierekezi, mdani wamkulu wa Mulungu, adagonjetsedwanso.

**Koma inu munandipangira ine choipa; koma Mulungu anachipangira chabwino ...** **Baibulo – Genesis 50:20**



# Baibulo long'ambidwa

Zaka makumi angapo zapitazo, panali malonda ogulitsa zinthu za m'nyumba mu mzinda wa wung'ono. Pakati pa izo panali Baibulo lalikulu lakale kwambiri, koma palibe amene anachita chidwi nalo. Pomaliza, wamalonda adapereka mtengo wotsika ndipo anali ndikuthekera kulitengera kunyumba pa ndalama zochepa.



Wogulitsa uyu malingaliro ake amafuna kugwiritsa ntchito masambawo kukulungira zomwe anali kugulitsa. Koma sanaganizire za mtengo wake wa masamba ambukuli. Mulungu wanena kuti: **"[Mawu anga] sadzabwerera kwa Ine chabe"** (Yesaya 55:11).

Mu mzindawu mudalinso munthu yemwe amakhala akuzunzika nthawi zonse poganiza kuti ali wolakwa chifukwa cha imfa ya munthu. Sanathe kupeza mpumulo usana kapena usiku. Mawu akuti "wakupha" nthawi zonse analikuyima pamaso pake m'malemba akulu. Tsiku lina anatumiza mwana wake ku shopu kuti akagule kena kake. Mwanayo adabwerako ndi chinthu anamutumacho chomwe chidakulungidwa patsamba la Baibulo lakaleli. Mwadzidzidzi panali vesi ili kuchokera pa Ahebri 9:22 pamaso pa munthu uyu: **"Popanda kukhetsa mwazi palibe chikhululukiro."**



Poyamba, mawu awa anali osamveka kwa iye. Komabe anali kufunafuna chikhululukiro. Amayenera kudziwa zochulukira za izi mulimonse. Choncho anatumizanso mwana wake kwa wamalonda, amene anali atayamba kung'amba masamba kuchokera ku Kalata yoyamba ya Yohane. M'mene bambo uyu amene anali kuzunzika ndi zolakwa zake anawerenga tsambalo, chipsinjo chonse chidatsikira pomwepo chifukwa adawerenga kuti: **"Mwazi wa Yesu Khristu Mwana wake utisambitsa kutichotsera uchimo onse"** ndi **"Ngati tivomereza machimo athu, ali Wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukire machimo athu ndikutisambitsa kutichotsera chosalungama chiri chonse"** (1 Yohane 1:7 & 9).

Mawu awa adawoneka ngati kuwala mu moyo wake wamdima. Anaona kuti mwazi wa Ambuye Yesu Khristu, womwe adakhetsa pamtanda, umatha kutsuka machimo onse. Kudzera mu izi, aliyense amene avomereza kulakwa kwake kwa Mulungu akhoza kupeza mtendere weniweni mu mtima mwawo ndi chikumbumtima chawo.

Mawu a Mulungu akhala m'dalitso kwa anthu zikwi zambiri. Nthawi zambiri imangokhala vesi limodzi kapena tsamba lochokera m'Baibulo. Mau a Mulungu "ndi amoyo ndipo amphamvu, ndi..... oboola" (Ahebri 4:12). Umu ndi momwe Mulungu "wagwedezera" mitima yambiri yowuma kapena yowonongeka.

Ngakhale Baibulo lomwe long'ambika limatha kutsogolera anthu ku njira yachimwemwe chenicheni ...

## Mawu A Mulungu Ndiye Choonadi

Mawu a Mulungu ndiye chowonadi. Amakhudza anthu mchikumbumtima chawo, ndikuwawonetsa pomwe alakwitsa, ndikuwapangitsa iwo kuti akhale osawutsika komanso osasangalala. Izi zimapangitsa kuti anthu ambiri azichita mantha ndi Baibulo ndipo chifukwa chake ena ayesetsa kuti alithetse.

## Mawu a Mulungu Adzakhala Kwamuyaya

Koma Mulungu amayang'anira Mawu Ake omwe ndipo sadzachoka.

**Sanjikizani pamodzi mabuku onse omwe amalankhula motsut-sana ndi Baibulo lina pamwamba pa linzake, ndipo mudzakhala ndi mulu wokwera kuposa mapiramidi a Giza. Kenako ikani Baibulo pafupi ndi muluwu. Baibulo silinena chili-chonse. Ndilopambana, ndipo limafotokoza zonse zomwe limadana nalo.**





**Koma mawu a Ambuye akhala kosatha.**

Baiulbo – 1 Petro 1:25

**Nthawi zonse, Yehova, mawu anu akhazikika kumwamba.**

Baibulo – Masalimo 119:89

**Chiwerengero cha mawu anu ndi chowonadi, Ndi maweruzo anu olungama onse akhala kosatha.**

Baibulo – Masalimo 119:160

# Baibulo lili ngati...

## Mkate



Mkate wotsika kuchokera kumwamba ndi uwu, kuti munthu adyeko ndi kusamwalira.
Yohane 6:50

## Moto



Kodi mawu anga safanana ndi moto? Atero Ambuye. Yeremiya 23:29

## Kuwunika

Mawu anu ndiwo nyali ya kumapazi anga, Kdi kuunika kwa panjira panga.
Masalimo 119:105



## Mkaka



Lirani monga makanda alero Mkaka woyenera, wopanda chinyengo, kuti mukakule nawo. 1 Petulo 2:2

## Uchi

... Lokoma koposa uchi ndi zakukha za zisa zake. Masalimo 19:10






## Golide

Ndizo zifunika koposa golide, inde, golide wambiri woyengetsa. Masalimo 19:10



## Siliva



Mawu a Yehova ndi mawu oona; Ngati siliva woyengedwa mu ng'anjo ya dothi ya Dziko lapansi, woyeretsedwa kasanu ndi kawiri. Masalimo 12:6

## Kalilore

Pakuti mawu a Mulungu ali ... kuwunika kwa malingaliro ndi zolinga za mtima. Ndipo palibe cholengedwa chobisika pamaso pake. Ahebri 4:12 & 13



## Nyundo



Kodi mawu anga....... sakhala ngati nyundo yomwe imaphwanya thanthwe mzidutswa? Yeremiya 23:29

## Lupanga

... lupanga la Mzimu, lomwe ndi mawu a Mulungu. Aefeso 6:17 ndi Ahebri 4:12



## Mbewu



[Mbeu] yosavunda... mawu a Mulungu a moyo ndi okhalitsa. 1 Petro 1:23

# Malangizo pa Kawerengedwe ka Baibulo

**Werengani Baibulo kuti mulumikizane ndi Mulungu mwachindunji. Mutha kuyamba, mwachitsanzo, ndi uthenga wabwino wa Luka mu Chipangano Chatsopano, nkhani ya moyo wa Yesu Kristu. Kuphatikiza apo, Chipangano Chatsopano ndichofunika kwambiri kuti timvetsetse Chipangano Chakale.**

**Ngati mukufuna kuwerenga Bayibulo ndi chisangalalo ndi phindu, mfundo zisanu ndi ziwirizi ndizothandiza:**

## 1. Gwiritsani ntchito matanthauziridwe (vesyoni) abwino

> Gwiritsani ntchito Baibulo lomveka, koma matanthawuzilidwe akhale pafupi fupi malemba akale.
(Tsoka ilo, pali matanthawuziridwe a Mabaibulo omwe munthu angapeze zolakwika kuchokera ku uthenga weniweni wa m'Baibulo.)

## 2. Pezani nthawi

> Tsimikizani kusiya theka labwino la ola limodzi tsiku lililonse kuti mukhale ndi "nthawi yakachete" kuti mukumane ndi Mulungu.
Tsiku lili ndi matheka a ola 96: perekani limodzi la iwo kwa Mulungu. Amafuna kulankhula nanu.

## 3. Mufunika chete

> Werengani Baibulo pamalo opanda phokoso
Zoonadi, mutha kuwerenga Bayibulo pa intaneti, kapena kutsitsa pulogalamu yaulele. Koma powerenga Baibulo ngati buku, simudzasokonezedwa ndipo mudzatha kuchita bwino kwambiri.

## 4. Pempherani kwa Mulungu

> Pemphani Mulungu kuti akuthandizeni kuti mumvetsetse zomwe mwawerenga.
Palibe amene angalongosole bwino za Baibulo kuposa Iye amene analemba.

> Funsani Mulungu: "Mukufuna kundiuza chiyani? Ndingazigwiritse ntchito bwanji? "
Iye yekha amawona mumtima mwanu ndipo amadziwa mavuto anu komanso momwe mukuvutikira.

> Thokozani Mulungu chifukwa cha Mawu Ake amtengo wapatali.
Kuwerenga Baibulo kumabweretsa madalitso komanso phindu lalikulu. Onani Masalimo 119:162

## 5. Lingalirani

> Ganizirani zomwe mwawerengazo.
Sizothandiza kwenikweni ngati mungangowerenga Baibulo mwachangu. Onani Masalimo 119:15 & 27 & 48

> Lembani mzere kunsi kwa m'mawu ofunikira ndi malemba ofanana.
Mukatero mudzawapeza mosavuta mtsogolo ndikuwakumbukira bwino.

## 6. Phunzirani pamtima

> Phunzirani pa mtima mavesi omwe akhala ofunika kwa inu.
Mutha kuwatchula mobwereza kwanthawi iliyonse. Choncho adzakhala othandiza kwa inu mu zochitika zosiyanasiyana m'moyo. Onani Masalimo 119:11, Akolose 3:16

## 7. Ziyikeni mu ntchito

> Chitani zomwe Mulungu akukuwonetsa ndikukuuzani m'Baibulo.
Kumvera Mulungu kumakupanga kukhala wokondwa komanso kumazamiitsa ubale wako ndi Iye. Onani Yakobo 1:22

**Odala ali iwo amene amva mawu a Mulungu, nawasunga.** Baibulo – Luka 11:28

# Kusankha kukufunika!

Mwalandira malingaliro ambiri komanso mauthenga ambiri okhudzana ndi Baibulo, “kalata” yochokera kwa Mulungu kwa inu. Chonde perekani yankho kwa Mulungu tsopano. Osakankha chisankho! Tsopano muyenera kuzindikira kuti ndikofunika kotani kumvetsera kwa Mulungu. Mwina simudzalandira mwayi wina.

Mulungu akufuna kubwera kwa inu mokoma mtima ndi chisomo osati ngati woweruza. Akukuyitanani kuti mutembenukire kwa Iye. Koma ngati mupitiliza kukhala opanda chidwi ndikukana uthenga wa Mulungu, kenako njira yanu ikukutsogolerani kuti mulekanitsidwe ndi Mulungu kwa muyaya, yomwe ndi Gahena.

**Koma Mulungu akupereka mphatso yamtengo wapatari kwa inu kudzera mwa Mwana wake, Yesu Khristu:**

**Mu pemphero kwa Mulungu, mutha kumasulidwa ku machimo anu onse ndi mawu osavuta komanso owona. Amakukhululukirani mosangalala mukamudziwitsa Iye . Muuzeni kuti mwakhala popanda Iye ndipo mwamuchimwira Iye. Ngati muchita izi moona, mutha kukhulupilira kuti Yesu Khristu adalipira mphotho ya machimo anu pamene adalowa mu ifa pa mtanda.**

**Ngati mungavomereze mphatso iyi yayikulu mwachikhulupiriro, njira yakumwamba idzakutsegukirani, malo amuyaya, chiyanjano chosangalala ndi Mulungu. Kenako moyo wanu udzakhala ndi cholinga komanso chofuna.**



Mulungu ali ndi chidwi chachikulu mwa inu. Chifukwa chake Iye akulankhula kwa inu kudzera mu m’kalata Yake, Bayibulo. Akufuna inu kuti mupulumutsidwe komanso kuti mulandire mtendere weniweni. Amakukondanidi ndi mtima wonse ndipo amasamala za inu.

Chonde werengani Baibulo mopanda kusamala komanso ndi mtima wotseguka. Muyankheni Mulungu! Muthokozeni Iye m’pemphero kuti Mawu Ake abwino abwera kwa inu, ndikuti mwawavomera. Ichi chidzakhala chisangalalo chachikulu koposa cha Mulungu!

**Kudzakhala chimwemwe kumwamba chifukwa cha wochimwa m’modzi wotembenuka mtima.**

Baibulo – Luka 15:7



Zingakhale zosangalatsa kwambiri kwa inu ngati mungathe kunena kwa Mulungu:

**Ndinavomera tchimo langa kwa Inu, ndipo mphulupulu yanga sindinaibisa. Ndidati, "Ndivomereza zolakwa zanga kwa Ambuye," ndipo Mwandikhululukiranso zoyipa zamachimo anga.**

**Baibulo – Masalimo 32:5**

Kenako malonjezo a Mulungu amuyaya adzagwiranso ntchito kwa inunso:

**… Ndizipatsa moyo wosatha,
ndipo sadzawonongeka konse;
ndipo palibe amene adzazikwatula
m'manja mwanga.**

Baibulo – Yohane 10:28

**Onani, Ine ndiri ndi inu masiku onse, kufikira chimaliziro cha zaka.**

Baibo – Mateyu 28:20



Apa mupezanso **"Kalata ya inu"** – ndi zowerenga zina zambiri – m'zilankhulidwe zambiri:

**BÍBLIAS & LIVROS CRISTÃOS**
Rua do Namaroi 13.433 – casa 309
Bairro da Liberdade (perto da Mesquita)
Matola – Maputo – MOÇAMBIQUE
+258 849 576 299 / +258 847 000 194
jesussalvador.dospecadores@hotmail.com

ou Caixa Postal 991, Correios Central
Av. 25 de setembro
Maputo – **MOÇAMBIQUE**

**CHRISTIAN AID AND LITERATURE AFRICA**
calamalawi@gmail.com · www.biblecenter-mw.com
P.O. Box 30809 · Lilongwe 3 · **MALAWI**

**Visit our Bible Centers in**

Lilongwe: Upland House, opposite Maula Mall, Area 3
Limbe: Opposite Limbe Police, Building No.2, after Puma filling station, From Illovo Round about
Dowa: Gospel Hall, close to Dzaleka school
Mzuzu: Close to Dynapham shop, right turn from SOSOSO bus depot to Mzuzu bus depot

ISBN 978-3-96162-195-8

GBV 195 4010 A Letter for You Chichewa